# Filipi tchati yophunzitsira za ECD kwa alezi m'sukulu za mmera mpoyamba




Sightsavers

# Za m'katimu


**Mawu oyamba** .......... 3

**Gawo la ndondomeko 1:** .......... 4
ECD ndi chani? Ndi chifukwa chiyani ECD ili yofunikira? Zoyenera kuti ophunzitsa ayang'anitsitse ndi kukumbukira

**Gawo la ndondomeko 2:** .......... 6
Kukula kwa mwana mzochita

**Gawo la ndondomeko 3:** .......... 8
Ndondomeko ya maphunziro a mmera mpoyamba ku Malawi – gawo loyamba

**Gawo la ndondomeko 4:** .......... 10
Ndondomeko ya maphunziro a mmera mpoyamba ku Malawi – gawo lachiwiri

**Gawo la ndondomeko 5:** .......... 12
Kulorerana ndi chani?

**Gawo la ndondomeko 6:** .......... 14
Zolepheretsa kulolerana

**Gawo la ndondomeko 7:** .......... 16
Kudziwa ndi kumvetsetsa za ulumali

**Gawo la ndondomeko 8:** .......... 18
Kudziwa zofooka ndi matenda osiyanasiyana

**Gawo la ndondomeko 9:** .......... 20
Kugwiritsa ntchito mawu osanyoza

**Gawo la ndondomeko 10:** .......... 22
Kulimbikitsa kupezeka ku sukulu za mmera mpoyamba

**Gawo la ndondomeko 11:** .......... 24
Kupanga sukulu za mmera mpoyamba kukhala zotetezeka kwa ana onse

**Gawo la ndondomeko 12:** .......... 26
Kuyang'anira ana kunja ndi mkati mwa sukulu za mmera mpoyamba

**Gawo la ndondomeko 13:** .......... 28
Zochitika mkalasi ya mmera mpoyamba

**Gawo la ndondomeko 14:** .......... 30
Kuwonetsetsa kuti ana olumala akutengapo mbali mu zochitika msukulu ya mmera mpoyamba

**Gawo la ndondomeko 15:** .......... 32
Kuwonetsetsa kuti mwana wa vuto la kuwona akutengapo mbali

**Gawo la ndondomeko 16:** .......... 34
Kuwonetsetsa kuti mwana wa vuto la kumva akutengapo mbali

**Gawo la ndondomeko 17:** .......... 36
Kuwonetsetsa kuti mwana waulumali wa ziwalo akutengapo mbali

**Gawo la ndondomeko 18:** .......... 38
Kuwonetsetsa kuti mwana amene ali ndi vuto lakuphunzira akutengapo mbali

**Gawo la ndondomeko 19:** .......... 40
Kulumikizana ndi kugwirira ntchito limodzi

**Gawo la ndondomeko 20:** .......... 42
Kukonza ndi kusatira ndondomeko yoyendetsera sukulu ya mmera mpoyamba

**Ndondomeko yoyendesera sukulu ya mmera mpoyamba** .......... 43

**Sources** .......... 44

**References** .......... 44



Filipi tchatiyi inalembadwa ndi Ronnie Stapleton, Guy Le Fanu, Betty Moses, Ben Chikaipa, Bright Chiwaula ndi Effie Kaminyoghe. Anajambula ndi Dan Amayo. Anamasulira ndi Ndongolera C. Mwangupili. Tithokoze mwapadera kwa Sightsavers Online and design team.

September 2019

# Mawu oyamba

Maphunziro awa ndi a alezi m'sukulu za mmera mpoyamba ku Malawi. Maphunzirowa alembedwa ngati ali pa pepala la pakhoma lomwe timalitcha filipichati.

Maphunzirowa akonzedwa kuti apereke nzeru ndi luso kwa alezi m'sukulu za mmera mpoyamba momwe akhoza kusamalira ana olumala m'sukuluzi.

Maphunzirowa ali ndi magawo a ndondomeko makumi awiri. Gawo la ndondomeko lililonse likuonapo mbali yake pa maphunziro a za mmela mpoyamba (ECD). Gawo la ndondomeko lililonse liyenera kutenga mphindi makumi atatu koma pali magawo a ndondomeko ena omwe atha kutalikirapo.

Pakuyenera kukhala munthu mmodzi oyendetsa gawo la ndondomeko lililonse. Munthuyo ayenera kukhala wodziwa bwino za mmera mpoyamba. Akhoza kukhala m'modzi wa alezi omwe anaphunzira za ECD. Ndizofunika kuti m'sabata limodzi aphunzire gawo la ndondomeko limodzi m'paka litamalizidwa. Koma ndizotheka kupanga magawo a ndondomeko onse mwakabwereza kapenaso kuwamaliza pamasiku angapo.

Tikawonesetsa tipeza kuti m'masamba aziwerengero zosagawika pawiri muli njira ya kuphunzitsa. Zithuzi ndi ndime ya mawu zofotokozera ophunzitsidwa zili m'masamba aziwerengero zogawika pawiri.

Mu filipitchati yonseyi mukamavundukula mupeze kuti zomwe mukufunika kuchita zaikidwa zizindikiro izi...

**Kufunsa:** ndiye kuti ophunzitsa atsogolere kukambirana pakati pa ophunzitsidwa.

**Kukambirana:** ndiye kuti ophunzitsa atsogolere kukambirana pakati pa ophunzitsidwa

**Kufotokoza:** ndiye kuti ophunzitsa afotokoze kwa ophunzitsidwa

- Ndiye kuti pali mndandanda wa mayankho omwe mukhoza kukambirana ndi ophunzitsidwa.

Zabwino zonse pamaphunziro anu! Kazigwiritseni ntchito zomwe mwaphunzira ku sukulu yanu ya mmera mpoyamba.

# Gawo la ndondomeko 1: ECD ndi chani? Ndi chifukwa chiyani ECD ili yofunikira? Zoyenera kuti ophunzitsa ayang'anitsitse ndi kukumbukira

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa adziwe khani za ECD
- Ophunzitsidwa adziwe ubwino wa ECD kwa ana

**M'gawo la ndondomeko ili muthandiza ophunzitsidwa kuti adziwe za ECD**

**1. Kufunsa:** Ophunzitsidwa akuziwa tathawuzo la malembo oti ECD?

- Malembo oti ECD akuyimila za mmela mpoyamba zomwe m'chizungu amati Early Childhood Development.

**2. Kufunsa:** Kodi ndi ana azaka zingati omwe ali m'gulu la ECD?

- Ndi ana omwe asanabadwe mpaka zaka zisanu ndi zitatu.

**3. Kufunsa:** Ndani amatengapo mbali paza ECD ndipo amapanga izi kuti?

- Makolo ndi achibale amatengapo mbali panyumba kwa ana asanabadwe mpaka zaka 8
- Alezi amapereka chithandizo kwa ana azaka zitatu mpaka zisanu m'sukulu za mmera mpoyamba
- Aphunzitsi a sukulu za pulayimale amapereka chithandizo kwa ana a zaka zitatu mpaka zisanu ndi zitatu (8)

**4. Kukambirana:** Cholinga cha ECD ndi chani? Wonetsani mawu omwe ali patsamba losatira. Mawuwo akutanthauza chani?

- Cholinga cha ECD ndi 'Kukhala ndi moyo', 'Kukula', 'Kukula mzochita', 'Chisamaliro', 'Chitetezo cha ana', 'Chilimbikitso', ndiponso 'Kutengapo mbali'.
- **Kukhala ndi moyo:** Izi zikutanthauza kukhala wamoyo. Mwana akhoza kukhala wamoyo ngati ali ndi zakudya ndi zakumwa zokwanira ndiposo ali wathanzi ndi osamalidwa.
- **Kukula:** Kukula kutanthauza kukhala wakulu ndi wamphamvu.
- **Kukula mzochita:** Kukula mzochita ndi kukhala ndi kuthekera kochita zithu. Tinganene kuti mwana wakula mzochitika akaphunzira kukwawa kenako kuyenda. Titha kunenanso kuti mwana wakula akaphunzira mawu achilendo ndikuyamba kumayakhulana ndi anthu. Ndiposo tingateronso tikawona mwana ataphunzira kudya yekha ndikusamba yekha ndi zina zotelo.
- **Chisamaliro:** Chisamaliro chimatanthauza kuwathandiza ana.
- **Chitetezo cha ana:** ichi chitanthauza kuti ana atetezedwa ku zinthu zomwe zikhoza kuwononga moyo wawo monga kuwazunza.
- **Chilimbikitso:** mwana akalimbikitsidwa amakula ochangamuka popanga zinthu. Mwachitsanzo, ngati mwana akamauzidwa nthano, amakula ndi mphamvu ya maganizo oyerekeza zithu.
- **Kutengapo mbali:** kutengapo mbali kumafuna kukhala munthu wojijirika. Mwana akamapanga zichitochitozi ndiye kuti akutengapo mbali.

**5. Kufunsa:** Kodi sukulu za mmera mpoyamba zingatengepo mbali yanji?

- Sukuluzi zingatengepo mbali ya **kukhala ndi moyo** ndi **kukula** poonetsetsa kuti mwana aliyese apeze madzi a ukhondo ndi phala tsiku lililonse.

**6. Kufunsa:** ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?

**Kutengapo mbali**

Kukhala ndi moyo

Chisamaliro

**Mmela mpoyamba**

**Kukula mzochita**

**Chitetezo cha ana**

Chilimbikitso

Kukula

# Gawo la ndondomeko 2: Kukula kwa mwana mzochita

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa akhoza kusonyeza masitegi osiyanasiyana omwe mwana amadusamo akamakula mzochita
- Ophunzitsidwa akhoza kusonyeza zomwe ana amatha kuchita mmasitegiwo
- Ophunzitsidwa akumvetsa kuti ana onse sakula mofanana


**1. Kufunsa:** Onani zinthuzi zomwe zili pa tsamba losatira.pakuwoneka ana anayi – khanda (osadutsa chaka chimodzi), mwana wophunzitsidwa kuyenda (wapakati pa chaka chimodzi kufikira zaka zitatu), mwana wopita ku sukulu ya mmera mpoyamba (zaka zitatu kufikira zisanu) ndi mwana woyamba sukulu ya pulayimale (zaka zisanu ndi chimodzi kufikira zisanu ndi zatatu).

| Magawo la ndondomeko osiyanasiyana | Ana akhoza kuchita izi |
|---|---|
| Khanda (osadutsa chaka chimodzi) | Amayang'ana nkhope; amayamba kumwetulira; amadziwa kuti awa ndi mawu kapena phokoso; amakweza mitu yawo; amatha kufikira zinthu; amayamba kupanga maphokoso osiyananasiyana; amayamwa zinthu; amagwira zinthu; amadya zakudya zowuma kapena zolimba; amakhala; amamera mano oyamba; amayamba kukwawa; amayamba kuyima modzikokera okha mmwamba;amalira akamamva njala kapena kuwawa; amafuna kudyetsedwa, kusintha ngakhalenso kufupatiridwa. |
| Mwana wophunzitsidwa kuyenda (kuyamba chaka chimodzi mpaka zitatu) | Amayamba kuyenda ndi kuyankhula; amadziwa ndikumva mawu ambiri; amadya ndi kuvala okha; amasewera; amamenya ndi kuponya mpira; amayamba zolembalemba; amalira akasiyidwa ndi munthu oti sakumudziwa |
| Wopita ku sukulu ya mmera mpoyamba (zaka zitatu mpaka zisanu) | Amapita ku sukulu ya mmera mpoyamba; amayankhula mziganizo; amayimba nyimbo; kulakatula; amajambula zinthu zodziwika; amadya okha;amayima ndikumayenda mopondera zala; amaponya mpira mwamphamvu; kudumpha ma sitepe aafupi; kumasula ma batani;kuyenda cham'mbuyo komanso mosata mzere; amathamanga komanso kudumpha |
| Mwana woyamba sukulu ya pulayimale (zaka zisanu ndi chimodzi mpaka zisanu ndi zitatu) | Amajowa; amathamanga kwambiri; kuvala komanso kuvula mosavuta; amamenya mpira ndi thabwa kapena mtengo; amajambula munthu oti ali ndi mutu, thupi komanso miyendo; amapanga malembo ndi kulemba dzina lake. Akakhala ndi zaka zisanu ndi ziwiri kupita kutsogolo, mwana ayenera kuchita zinthu zokhwimirapo monga kuvina, kulumikiza chithunzi chodulidwa mozwetazweta, kujambula zinthu mwa dongosolo |

**2. Kukambirana:** ana amayenera kuchita chiyani mmasitejiwa?

- Ana amafika gawo lina lake ndikumachita zinthu akakwanisa zaka zina zake. Atha kuchita chinthu china chake ali zaka ziwiri chomwe anakanika kuchita ali ndi chaka chimodzi, komanso atha kuchita chinthu ali zaka zitatu chomwe anakanika kuchita ali ndi zaka ziwiri.
- Koma ana ndiosiyana. Ana onse amakula mosiyana mu nthawinso yosiyana. Funsani ophunzitsidwa kuti aganizire kusiyana kwa ana awo omwe kapena ana omwe akuwadziwa ndipo adzazindikira zomwe mukuthandauza.
- Ana ena amaulumali amakula mochedwerako muzinthu zina kusiyana ndi ana ena. Muyenera kuzindikira chimenecho ndikuyesesa kuwathandiza mmene mungathere kuwathandiza. Kumbukiraninso kuti ana olumala amadzawapeza anzawo aja pakadutsa kanthawi. Komanso ana ena olumala amatha kukula kapena kuphunzira zinthu zina mwa changu kuposa ana ena. Mwachitsanzo, mwana woti ayenera kugwiritsa ntchito njinga za olumala atha kuphunzira mwachangu.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 3: Ndondomeko ya maphunziro a mmera mpoyamba ku Malawi – gawo loyamba

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa apereke magawo atatu a kuphunzira
- Ophunzitsidwa afotokoze kuti gawo lililonse mwa atatu atchulidwawo likukhudzana ndi chani

**1. Kufotokoza:** Ndondomeko ya maphunziro a mmera mpoyamba ndiyovomerezeka ndi boma la Malawi kuzera mu unduna woona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amuna ndi akazi, ndi chisamaliro cha ana ndi olumala.

Ndondomekoyi ili ndi magawo asanu ndi limodzi akuphunzira. Ndondomekoyi imayikilatu zofunika kuchita pa gawo lililonse.

Ophunzitsidwa azikambirana za magawo atatu mu phunziro ili. Magawowa nawo: Gawo la lokhuzana ndi thupi; Gawo la chikhalidwe komanso kaganizidwe.; Njira zosiyanasiyana zophunzirira.

**2. Kufotokoza:** Wonani zithunzi zomwe zili pa tsamba losatira. Gulu lililonse la zithunzizo likuyimira gawo la kuphunzira.

**3. Kukambirana:** Gawo lokhuzana ndi thupi. Kodi zithunzizo zikuonesa chani pa kakulidwe?

- Ana amaonesa luso la zochitachita zofuna mphamvu (makamaka pochita zinthu zazikulu) – mwachisanzo, kulumpha.
- Ana amaonesa luso la kuganiza (makamaka pochita zinthu zocheperako) – mwachisanzo, kulemba.
- Ana amaonesa nzeru zochita zinthu mwa dongosolo; mwachitsanzo, kusiyanisa zinthu nthawi imodzi.
- Ana amagwiritsa ntchito mphamvu zonse zisanu (za kununkhiza, kugwira, kulawa, kumva komanso kuwona) pofuna kudziwa zinthu za mdziko.

**4. Kukambirana:** Gawo la kukula mu chikhalidwe ndi kaganizidwe. Kodi zithunzizo zikuonesa chani pa kakulidwe ka chikhalidwe ndi kaganizidwe?

- Ana akuwonesa kudziwa kochitira zinthu pamodzi komanso kuthandizana.
- Ana akuonesa kuthekera kochita ubale ndi anzawo, komanso akulu.
- Ana akupatsidwa mpata woonesa mmene akumvera komanso mmene akuganizira, nthawi yomweyonso akuphunzira kuledza mtima.
- Ana akuonesa kuti akuphunzira bwino ali aang'ono. Ichi chikuwachititsa kukhala osangalala komanso odzikhulupirira.

**5. Kukambirana:** Njira zosiyanasiyana zophunzirira. Zithunzizo zikuonesa chani pa njira zosiyanasiyana zophunzirira?

- Ana akupatsidwa mwayi kuphunzira mwanjira zosiyanasiyana – izi zikuchititsa kuti azikhala odzikhulupirira komanso amatha kuphunzira ma luso osiyanasiyana.
- Ana akupatsidwa mwayi kuwonesa zomwe anaphunzira kale kudzigwiritsa ntchito pa zomwe zikuchitika nthawiyo (mwachitsanzo, azifananisa zomwe zikuchitika mu nkhani ndi zomwe anaphunzira ndi kudziwa tsiku lina).
- Ana amalimbikitsidwa kuti adzikhala opilira ndi kudekha pamene akufuna kudziwa zithu za mdziko (mwachisanzo, mwana ayenera kuthirira chomera pafupipafupi ngati akufuna chomeracho chikule).
- Ana amayamba kusankha okha zomwe akufuna kuphunzira (mwachitsanzo, ana amaganiza okha zomwe akufuna kuwumba).

**6. Kufotokoza:** Ana apatsidwe mwayi kuti aphunzire ndikudziwa ma gawo onse a kuphunzira. Akumbutseni ophunzitsidwa kuti ana ena atha kumavutika kuphunzira magawo ena. Ndi ntchito ya osamalira ana kukhala wodekha, wothandizira komanso wolimbikisa.

**7. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?


1 2 3 4 5 6
1 + 1 = 2
2 + 2 = 4
3 + 3 = 6
Aa
Bb
Cc
Dd
Ee
1
4
5
6
7

# Gawo la ndondomeko 4: Ndondomeko ya maphunziro a mmera mpoyamba ku Malawi – gawo lachiwiri

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa adziwe ma gawo atatu omaliza a kudziwa kapena kuphunzira
- Ophunzitsidwa athe kufotokoza zomwe gawo lilonse likunena

**1. Kufunsa:** Ophunzitsidwa anene magawo atatu a kuphunzira omwe afotokozedwa pa phunziro lomwe linachitika?

**2. Kufotokoza:** Magawo atatu omwe afotokozedwe ndi awa: Chiyankhulo, kudziwa kulemba ndi kuwerenga komanso luso la kuyankhulana; Kudziwa komanso nzeru zosiyanana; kukula mu chikhalidwe komanso uzimu.

**3. Kufotokoza:** Chiyankhulo, kudziwa kulemba ndi kuwerenga komanso luso la kuyankhulana. Gawo ili ndilokhuza zinthu izi:

- Ana kufotokoza zomwe akudziwa ndi kuganiza.
- Ana kusewera pamodzi kuti apititse patsogolo luso loyankhulana.
- Ana kupatsidwa mwayi woti aziwerenga, kulemba ma kalata ndi kudziwa zokhuza ma buku.

**Kufunsa:** Wonani zithunzi zomwe palinso mayi ndi mwana akuphika limodzi. Kodi zithu zomwe zajambulidwazo zingathandizire bwanji kuti mwana adziwe chiyankhulo, kulemba, kuwerenga komanso kuyankhulana ndi anthu ena?

**4. Kufotokoza:** Kudziwa komanso nzeru zosiyanasiyana. Gawo ili limakhuza zinthu izi:

- Ana kupatsidwa mwayi woganiza za zinthu za mdziko
- Ana kupatsidwa mwayi wopeza mayankho a zovuta zinazina.
- Ana kupatsidwa mwayi kuti anene zomwe akudziwa komanso kugawana ndi anzawo zithu zomwe akudziwa.

**Kufunsa:** Wonani zithunzi pomwe palinso chithunzi cha mwana akuwerenga zotsekera pa botolo la fanta. Kodi zomwe zajambulidwazo zingathandizire bwanji kuti mwana akhale odziwa komanso kukhala ndi nzeru pa zinthu zambiri?

**5. Kufotokoza:** Kukula mu chikhalidwe komanso uzimu. Gawo ili limakhudza zithu izi:

- Kulimbikitsa ana kuti azidzisamala komanso kulemekezana.
- Kulimbikitsa ana kuti adziwe kufunika kwa malamulo komanso chikhalidwe.
- Kulimbikitsa ana kuti athe kuzindikira chithu chabwino ndi choyipa.

**Kufunsa:** Onani zinthuzi zomalizazo. Kodi zimenezi zikuthandizira bwanji kuti ana akule pa chikhalidwe komanso mu uzimu?

**6. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 5: Kulorerana ndi chani?

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa afotokoze tanthauzo la mau oti 'kulorerana pa maphunziro'
- Ophunzitsidwa afotokoze kuti ndi chifukwa chani ana omwe ali ndi maulumali ali ndi ufulu wa maphunziro osasalana komanso mzochitika za mmera mpoyamba mosasalidwa
- Ophunzitsidwa afotokoze ngati ana olumala mmidzi yawo amapatsidwa maphunziro osasalana kuphatikizapo ntchito za mmera mpoyamba

**1. Kufotokoza:** Ophunzitsidwa azikambirana mau oti **kulorerana** komanso **kulorerana pa maphunziro**. Lembani mawu amenewa pa chipepala chachikulu kapena pa bolodi kuti aliyense azitha kuwona.

**2. Kufunsa:** Wonani zithunzi zomwe zili patsamba lotsatira. Chikuchitika ndi chani muzithunzizo?

**3. Kufotokoza:** Anawa

- **Akupezeka** – alipo akupezeka/abwera.
- **Akutengapo mbali** – ali tchelu ndipo akutengapo mbali.
- **Akukwanirisa** – akuphunzira luso ndi nzeru zatsopano kumanso kudziwa kuthekera kwa zinthu zatsopano (monga kupanga ubale ndi anzawo).
- **Kulorerana** kumathandauza kuti kupezeka, kutengapo mbali komanso kukwanirisa, zonse zikhalepo.[2]

**4. Kufotokoza:** Ntchito za mmera mpoyamba zololerana nzotheka pokhapokha pali **kupezeka, kutengapo mbali** komanso **kukwanirisa**

Izi zikuthandauza kuti ana onse kuphatikizapo olumala ayenera kuti:

- Apezeke mmasukulu a mmera mpoyamba (CBCC) kumaphunzira limodzi ndi ana ena.
- Azitengapo mbali yayikulu mzochitika za sukulu za mmera mpoyamba limodzi ndi ana ena.
- Kukwanirisa mzochitika za ku sukulu ya mmera mpoyamba – kuphunzira luso ndi nzeru za tsopano komanso kupanga abwenzi atsopano

**5. Kufotokoza:** Ana olumala mMalawi ali ndi ufulu wa maphunziro osasalana komanso apamwamba kuphatikizapo sukulu za mmera mpoyamba ngati ana ena onse. Ufulu umenewu ndiwotetezedwa ndi phangano la nthambi ya bungwe la maiko onse la United Nations lowona za ufulu wa ana olumala (United Nations Convention on the Rights of Persons with Disabilities-2006). Dziko la Malawi linasayinira nawo phangano limeneli.

**6. Kufunsa:** Ayikeni Ophunzitsidwa akhale awiriawiri kapena akhale mmagulu ang'onoang'ono.

Afunseni aganizile za ana olumala mmidzi yawo. Kodi anawa akupita nawo ku sukulu za mmera mpoyamba?

- **Amapezeka** m'sukulu za mmera mpoyamba? Ngati amapezeka...
- **Amatenga nawo mbali** mzochitika za ma sukuluwa?
- Kodi **akukwaniritsa** china chake ku sukuluzi?

Gulu lililonse liyenera kufotokoza kwa onse zomwe lapeza kapena lakambirana.

**7. Kufunsa:** Kodi ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 6: Zolepheretsa kulolerana

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa adziwa zolepheretsa kapena zopsinja kuchitira limodzi ntchito za mmera mpoyamba pakati pa ana a ulumali ndi a lungalunga
- Ophunzitsidwa akutha kunena njira zothetsera zoletsanzo

**1. Kufotokoza:** Ophunzitsidwa akambirane za zoletsa zomwe zimakhalapo kuchitira limodzi ntchito za mmera mpoyamba.

**2. Kufunsa:** Chipsinjo kapena chiletso ndi chani?

- Chiletso ndi chopsinja, chithu chosokoneza kapena kulepheresa kuchita chinachake.

**3. Kufunsa:** Nenani zipsinjo zomwe zitha kulepheretsa ana olumala kutenga nawo mzochitika za sukulu za mmera mpoyamba. Lembani zipsinjozi pa pepala lalikulu (filipichati) kapena pa bolodi.

**4. Kukambirana:** Zipsinjozi ndi izi: gwiritsani ntchito zojambula za pa tsamba lotsatira kuti zikuthandizeni kufotokoza kwake.

- **Makhalidwe ndi maganizo oipa** zomwe timachitira anthu ulumala (kulorerana kapena kusalana). Aphunzitsi, anthu onse mmidzi ndi ana opanda ulumali atha kumaona ngati ana olumala ndiosafunikira kwambiri kapena kuti ndi osalira kuyerekeza ndi ana ena. Atha kumakhala ndi mantha kapena kusakondwa akaona mwana olumala. Makolo a ana olumala nawonso atha kumaona choncho ndikumachita manyazi chifukwa chokhala ndi ana olumala.
- **Kutalika kwa mtunda kuchokera ku sukulu ya mmera mpoyamba.** Mwachitsanzo, ana olumala atha kuvutika kuyenda kupita ku sukuluzi ngati mtunda wake ndiwautali, ngati njira yake ndiyokumbika, ngati pali makwawa ofuna kudutsa komanso ngati misewu muli anthu kapena magalimoto ambiri kapena ndiyovuta kuwoloka. Ana omwe ali ndi vuto la maso (vuto la kuwona) ndi ana olumala atha kuvutika poyenda kupita ndi kuchoka ku malo a mmera mpoyamba.
- **Kafikilidwe ka malo a sukulu za mmera mpoyamba.** Mwachitsanzo, malowa atha kukhala ndi ma sitepe ndi tinjira tating'ono (zomwe zimapereka mavuto kwa ana olumala). Zimbuzi nazonso zitha kukhala vuto kuti anawa afikire.
- **Kusowa kwa zipangizo ndi ndalama.** Mwachitsanzo, malowa atha kukhala osowekera zipangizo zophunzitsira ndi kuphunzirira komanso ana olumala atha kusowekera zipangizo zowathandizira monga njinga zoyendera ndi ndodo zoyendera anthu olumala.
- **Kudwala.** Ana ena olumala atha kukhala ndi matenda omwe oti amawapangitsa kujomba ku sukulu kamba kodwala.
- **Kusiyana pakati pa ana aamuna ndi aakazi.** Ana atsikana omwe ali ndi ulumali ndiomwe amakhala pachipsinjo kwambiri kupita ku sukulu kusiyana ndi anyamata omwe ali olumala. Funsani ophunzitsidwa mbali kuti afotokoze kuti zinthu zimakhaliranji choncho.

**5. Kufunsa:** Mmagulu kapena awiriawiri, ophunzitsidwa apeze njira zothetsera mavutowa. Gulu lililonse lisankhe chopsinja chimodzi. Mwachitsanzo, kaganizidwe ndi zikhalidwe zoipa zingathe ngati anthu mmidzi angaphunzitsidwe kapena kudziwitsidwa.

**6. Kufunsa:** Akamaliza kukambirana, afotokoze kwa gulu lonse zomwe apeza. Perekani mwayi kuti pakhale kukambirana kwakukulu pa nkhani yothetsa zipsinjozi.

**7. Kufunsa:** Anthu aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 7: Kudziwa ndi kumvetsetsa za ulumali

## Zotsatira

- Ophunzitsidwa adziwa liwu loti kulumala
- Ophunzitsidwa adziwa olumali osiyanasiyana

### 1. Fotokoza

- Ana atha kukhala ndi zofooka ndi matenda osiyanasiyana
- Zofookazi pamodzi ndi matendawa zitha kubweretsa ulumali – kulumala kumatanthauza kupezana ndi mavuto kapena zipsinjo pophunzitsidwa pa zochitika. Kulumala kumabweranso kamba ka kaganizidwe koipa ndi zikhalidwe zoipa.

### 2. Kufunsa: Wonani mndandanda wa zofooka ndi matenda pa tsamba lotsatira. Ophunzitsidwa afotokoze kuti mawu omwe ali pamenepo akuthandauza chani.

- Vuto la kumva: Mwana amene ali ndi vuto lakumva amava pang'ono kuyerekeza ndi anzake, komabe amamva. Ana ena atha kumva pang'ono kwambiri kapena osamva ndikomwe. Zikatero mwana uja ndiye kuti ndi wogontha.
- Vuto la kuwona: Mwana wa vuto la kuwona amawona pang'ono kuyerekeza ndi ana ena, komabe amaona. Zikatere timati mwana amaona pang'ono. Pena mwana amaona pang'ono kwambiri kapena sawona nkomwe. Pamenepo timati mwana ndi wa khungu.
- Kugontha ndi khungu: Mwana amene samamva koma sawona ndiye kuti ndi wogontha komanso wa khungu.
- Ulumali wa ziwalo za miyendo ndi manja: Mwana amene ali ndi vuto lalikulu kusuntha ziwalo zina za thupi lake (mwachitsanzo miyendo, manja) ndi olumala.
- Ulumali wa ubongo: Izi zikuthandauza kuti mwana ali ndi vuto lalikulu mu kaganizidwe, kuphunzira komanso kupeza mayankho pa mavuto ena ndi ena. Ndi ana ochepa chabe omwe ali ndi ulumali otero. Ngati mwana ali ndi zovuta zochepa kutsatira zomwe akuphunzira, ngati akusalira pang'ono, sizikuthandauza kuti ndi olumala mu ubongo, koma chabe kuti akupezana ndi vuto lina laling'ono mmaphunziro awo lomwe mutha kuthandizirapo.
- Ulumali wofooka kapena kuuma kwa ziwalo: zikuthandauza matenda omwe amachitisa kuti munthu akhale ndi vuto la kuyenda ndi kulumikiza zinthu mwa dongosolo. Vuto ili limabwera chifukwa cha kuvulala kwa ubongo pa nthawi yoti mwana sanabadwe, kapena yobadwa kapena atabadwa kale. Ngakhale zili choncho, ana amanjenje amakhalabe anzeru zakuya ngakhale kuti amakhala ndi vuto loyenda.
- Vuto la kuyankhula Awa ndi mavuto omwe amachitisa kuti mwana asamayankhule zinthu zomveka bwino akamayankhula.
- Kulumala kophatikizana Awa ndi ma ulumali ambirimbiri mophatikiza; mwachitsanzo mwana atha kukhala ndi vuto la kumva komanso vuto loyenda.
- Khungu la chi alubino izi zimachokera kwa makolo pobadwa. Ana a khungu la chi alubino amakhala ndi khungu loyera kwambiri kusiyana ndi anzawo, komanso amaona movutika. Samafunika kukhala pa dzuwa lowala kwambiri ndipo ayenera kutetezedwa ku dzuwa la chonchi.

### 3. Fotokoza

- Ana onse kuphatikazapo olumala ali ndi ufulu wopita ku sukulu za mmera mpoyamba.
- Ana onse kuphatikizapo olumala atha kumakhonza bwino ku sukulu za mmera mpoyamba.
- Ngati mukugwira ntchito ndi mwana olumala, limbikirani kuchita zomwe mwanayo akutha kuchita, osakhala zomwe akukanika
- Ndizofunika kwambiri kuyesesa kudziwa zofooka za mwana. Mukatero mutha kupeza njira yabwino yomuthandizira.

### 4. Kufunsa: Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?

Ulumali wa ziwalo za miyendo ndi manja

Khungu la chi alubino

Vuto lakumva

Vuto la kuwona

Vuto la kuyankhula

Ulumali wa ubongo

Ulumali wofooka kapena kuuma kwa ziwalo

Kulumala kophatikizana

# Gawo la ndondomeko 8: Kudziwa zofooka ndi matenda osiyanasiyana

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa adziwa ana omwe ali ndi zofooka ndi matenda kapena omwe ali pa chiopsezo chokhala ndi zofookazo

**1. Kufunsa:** Wonani zithunzi zomwe zili pa tsamba lotsatira. Kodi anawa ali ndi zofooka zotani?

- Mwana woyamba ndi wosawona.
- Mwana wachiwiri wavala magalasi. Izi sizikuthandauza kuti mwanayu sakuwona. Ngati mwanayo akuwona bwino atavala magalasi ndekuti alibeso vuto lowona. Ngati mwana ali ndi vuto powona, ngakhale akhale atavala magalasi, mwanayo adakali wa vuto la kuwona.
- Mwana wa chitatu ali pa njinga ya anthu olumala. Ameneyo ndi olumala.
- Mwana wachinayi akufuna ndondo zoyendera. Iyenso ndi olumala.
- Mwana wa chisanu ali ndi khungu la chi alubino.

**2. Kufotokoza:** Nthawi zina sizimavuta kudziwa ana omwe ali ndi mavuto kapena zofooka zosiyanasiyana kapena omwe ali pachiopsezo choti zofookazo zitha kuwapeza. Nthawi zina kudziwa kumavuta.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa afotokoze zizindikiro zomwe angaone ponena kuti mwana ali ndi ulumali? Nazo zizindikilozi:

- Amadzimenyetsa ku zinthu kapena kuzigwera zinthuzo.
- Maso awo amaoneka mosiyana ndi a ana ena; mwachitsanzo, maso awo amakhala ofira, kapena mwamadzimadzi kapena okhalala.
- Amafikisa maso kapena kuphetiraphetira.
- Samayankha munthu akayitana dzina lawo.
- Satengapo mbali pa ntchito za mkalasi kapena amachita kukakamizidwa kutero.
- Amavutika kapena kukanika kusuntha manja kapena miyendo.
- Samaphunzira mwachangu kufananiza ndi ana ena.
- Amavutika kuchoka pamalo kupita pena.
- Sakonda zoyankhula; pena sayankha kumene.
- Nthawi zambiri amakhala osakondwa, wobalalika komanso okwiya.
- Nthawi zambiri amakhala odwala, mwachitsanzo, chifuwa, chimfine choti chimaoneka kuti sichitha.
- Nthawi zambiri amajomba ku sukulu za mmera mpoyamba.
- Amakhala ndi anzawo ochepa ndipo nthawi zambiri amakhala paokha.

**4. Kufotokoza:** Osamala anawa ayenera kuwawonesesa anawa ku sukulu za mmera mpoyamba kuti athe kuona zizindikiro ngati mwana ali ndi zofooka zosonyeza ulumali.

- Ngati akuwona kuti mwana ali ndi zofooka zoonesa ulumali, akambirane nkhaniyo ndi makolo amwanayo.
- Ana ayenera kupititsidwa ku chipatala kuti akawunikidwe bwino komanso kuti ngati pangakhale chithandizo chotsatira, mwachitsanzo, mwanayo atha kufunika chithandizo chochiza vutolo kapena thandizo lina monga njinga zoyendera olumala.
- Ndikoyenera kudziwa zambiri za mmene mwana alili kuti mwanayo azithandizidwa bwino ku sukulu za mmera mpoyamba.

**5. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 9: Kugwiritsa ntchito mawu osanyoza

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa adziwa mawu onyoza omwe anthu mmidzi amagwiritsa ntchito ponena za ana olumala komanso adziwa chifukwa chomwe sibwino kugwiritsa ntchito mawu otere.
- Ophunzitsidwa adziwa kugwiritsa ntchito mawu olemekeza ana olumala.

**1. Kufotokoza:** Ana olumala ali ngati ana ena onse, chabe iwowo ali ndi mavuto mzochita zina ndi zina monga kumva, kuwona, kumvetsetsa, kuyenda ndi zina zotero. Ndi thandizo lanu komanso thandizo la enanso, anawa atha kukhala ndi kuphunzira mwansangala m'sukulu za mmera mpoyamba.

**2. Kufotokoza:** Nthawi zina anthu amagwiritsa ntchito mawu osapereka ulemu kwa anthu olumala kuphatikizapo ana olumala.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa apereke mdandanda wa mawu onyoza omwe anthu mmidzi amagwiritsa ntchito pokamba za ana olumala. Lembani mawuwo Pa filipichati kapena pa bolodi.

**Kufotokoza:** Kuyankhula kwa choncho ndikosavomerezeka ndipo kusamachitike.

- Tsindikani kuti (a) kuyankhula kwa choncho ndikonyoza komanso kopweteka (b) kumachititsa anthu ena kuchitira zoipa anthu olumala.
- Tsindikani kuti munthu akamayankhula ndi mwana wolumala, adzimutchula dzina lake loyamba ngati mwana wina aliyense.

**4. Kufotokoza:** Akamakambirana zokhuza ana olumala m'sukulu za mmera mpoyamba, adzigwiritsa mawu osanyoza ana. Mwachitsanzo, mmalo monena kuti 'alubino', azinena kuti 'wa khungu la chi alubino', Mmalo monena kuti wa 'khungu', anene kuti 'mwana wa vuto losawona'. Mmalo monena kuti 'wopunduka', anene kuti 'mwana amene ali ndi ulumali'.

**5. Kufunsa:** Wonani mndanda wa mawu omwe uli pa tsamba lotsatira ndipo afunseni apereke mawu abwino osanyoza ana.

- Mtsikana wa khungu la chi alubino
- Mnyamata wa vuto losawona
- Mwana wa ulumali wa ziwalo za miyendo ndi manja
- Mwana wa kulumala kophatikizana
- Mtsikana wokanika kuyenda
- Mnyamata wa ulumali wa ubongo ndi ziwalo za thupi
- Mwana wokanika kugwiritsa ntchito dzanja la manja
- Ana a vuto lowona

**6. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?

## Ikani izi mu chiyankhulo cha bwino chofotokoza za olumala

| | Mtundu wa Ulumali |
|---|---|
| Mtsikana | Khungu la chi alubino |
| Mnyamata | Kusawona |
| Mwana | kulumali wa ziwalo za miyendo ndi manja |
| Ana | kulumala kophatikizana |
| Mtsikana | Sakuyenda |
| Mnyamata | Kulumala kwa ubongo ndi ziwalo za thupi |
| Mwana | Akukanika kugwiritsa ntchito dzanja la manja |
| Ana | Kusawona |

# Gawo la ndondomeko 10: Kulimbikitsa kupezeka ku sukulu za mmera mpoyamba

## Zotsatira:

- Alezi atha kupereka njira zosiyanasiyana mmene angathe kulimbikitsa ana olumala kuti azipezeka ku sukulu za mmera mpoyamba

**1. Kufunsa:** Wonani zithu za alezipa tsamba lotsatila. Kodi iwowa mzithunzinzo akugwiritsa njira zanji polimbikitsa kupezeka kwa ana olumala m'sukuluzi?

- Kuyankhula ndi makolo.
- Kupalasa njinga kupita ku sukulu atanyamula mwana kumbuyo.
- Kuwonesa mwana malo ozungulira sukulu ya mmera mpoyamba
- Mwana olumala adziwane ndi anzake.

**2. Kufunsa:** Ophunzitsidwa apereke njira zosiyanasiyana mmene angathe kulimbikitsa ana olumala kuti azipezeka ku sukulu za mmera mpoyamba. Lembani mfundo zomwe apereka pa filipichati kapena pa bolodi

- Kukumana ndi anthu mmidzi kuti awone ngati pali ana ena olumala amene sakumapita ku sukulu za mmera mpoyamba
- Kukonza tsiku loti makolo ndi anthu mmidzi apite ku sukulu za mmera mpoyamba kuti akawone zinthu zomwe zimachitika m'sukuluzi.
- Kuyendera makolo ku nyumba zawo nkumawalimbikitsa kuti apitise ana awo ku sukulu'zi.
- Kukumana ndi makolo pafupipafupi mwana wawo akayamba kupita kusulu'zi
- Kupeza nthawi kuyankhulana ndi mwana olumala maso ndi maso payekha.
- Kukumana ndi osamalira ana anzanu kukambirana ndi kumanga mfundo zolimbikitsa kuti ana olumala azipezeka nawo ku sukulu'zi.
- Kukambirana ndi alangizi a boma monga ogwira ntchito zoteteza ana ndi olimbikitsa ukhondo mmidzi.
- Kuthandiza ana olumala kupita ku sukulu komanso kubwerera kunyumba powakonzera mayendedwe.
- Kulimbikitsa chikondi ndi ubale pakati pa ana olumala ndi ana ena onse.
- Kuwonetsetsa kuti ana onse, kuphatikizapo olumala, akulandira chakudwa ku sukulu za mmera mpoyamba.
- Kuwonetsetsa kuti ana olumala akupatsidwa mpata osewersa zithu zopezeka ku sukulu'zi monga siso, zozendewera ndi zina.
- Kuwonetsetsa kuti ana onse kuphatikizapo olumala akutenga nawo mbali pa masewero ndi zochitika zosiyanasiyana pa sukulu.
- Kuwachitira zinthu zabwino ana onse pamodzi ndi olumala komanso kumawaonetsa chikondi.
- Kukonza nyumba, njira ndi zinthu zotero pa sukulu kuti ana olumala asamapezane ndi mavuto monga kulowa mkalasi.
- Kukongoletsa makhoma a sukulu'zi kuti malo ophunzirira azipereka chikoka kwa ana.

**3. Funsani:** Kodi ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 11: Kupanga sukulu za mmera mpoyamba kukhala zotetezeka kwa ana onse

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa anene zinthu zomwe akuona kuti zikupereka chiopsezo kwa ana pa sukulu
- Ophunzitsidwa apange ndondomeko yochotsera zinthu zooopseza chitetezo cha ana pa sukulu yawo
- Ophunzitsidwa ayambe kugwiritsa ntchito ndondomekozo

**1. Kufunsa:** Wonani zithunzi za mkati komanso kuja kwa sukulu ya mmera mpoyamba pa tsamba lotsatira.

- **Tchulani ziopsezo zopezeka kunja kwa sukulu.** Mwachitsanzo: miyala yaikulu yomweyitha kugwetsa ana, mitengo yodula mmbali mwa ma kalasi, kalasi loti polowera pali ma sitepe akuya, zoseweretsa zoti zili ndi zitsulo zozendewera mmalele, zinyalala, ma galasi osweka, nkhwangwa yoti yangotsiyidwa pansi, madzi odontha kuchoka mu thanki.
- **Tchulani ziopsazo za mkati mwa sukulu** Mwa chitsanzo: mabokosi oti atha kugwetsa ana, zidole zoti zangoponyedwa pansi, chitseko choonongeka, ma galasi osweka, zidole zoonongeka, mabotolo osweka ndi zina zotero

**Kufotokoza:** Zinthu izi zikuopseza chitetezo cha ana onse, osakhala olumala okha.

**2. Kufunsa**: Onse aleziamene akutengapo mbali pa maphunziro awa ayende kuzungulira sukulu komanso kulowa mkati. Alembe zoopseza chitetezo cha ana zomwe akuwona. Pamodzi, onse alembe ndondomeko yomwe angasate powonetsetsa kuti pa sukulu pali chitetezo chabwino cha ana. Ayenera kutchula zinthu izi:

- Chomwe chiyenera kuchitika ndi chani?
- Amene achite ntchitoyo ndani? (mwachitsanzo, osamala ana, makolo, anthu onse mmudzi)
- Nanga ntchitoyo yigwiridwa motani?
- Ntchitoyo yigwiridwa liti?
- Pafunika chani (anthu, zipangizo, ndalama) ndipo zichokera kuti?

**3. Kufotokoza:**

- Aleziawonetsetse kuti ntchito zonse mkati ndi kunja komwe ndizosapereka chiopsezo kwa aliyense.
- Awonetsetse kuti malo apa sukulu za mmera mpoyamba pasakhale chiopsezo chilichonse.
- Zipangizo zosewerera panja ziyenera kuwonedwa ndi kutsimikizika kuti zili bwino sizingapereke chiopsezo kwa ana.
- Zofuna za mwana komanso kaganizidwe kake ndizofunika chimodzimodzi ndi zofunika za chitetezo cha ku thupi. Ngati osamala ali nkhawa zina zake pa zofuna ndi kaganizidwe ka mwana, ayenera kupita kukafunsa uphungu kwa ogwira ntchito zoteteza ana.
- Ngati mwana ali pa vuto la za umoyo kapena kunyentchera, aleziayenera kukambirana ndi makolo ndikuonesetsa kuti mwana walandira chithanzi choyenera. Ngati makolo sakuchitapo kanthu, aleziali ndi udindo wopita kwa ogwira ntchito za chipatala mdera kuti athandizepo.
- Aleziapewe kunyamula ana olumala pokhapokha a za chipatala kapena makolo awaphunzitsa mmene angawanyamulire.

**4. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 12: Kuyang'anira ana kunja ndi mkati mwa sukulu za mmera mpoyamba

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa azitha kunena kufunikira koyang'anira ana kuja ndi mkati mwa sukulu za mmera mpoyamba
- Ophunzitsidwa azitha kufotokoza njira zoyenera zogonjesera mavuto omwe amapezeka

**1. Kufunsa:** Onani zithunzi pa tsamba lotsatira. Afunseni anene malo omwe aleziakuyang'anira ana komanso chifukwa chani akuwayang'anira.

**Kufotokoza:** Ndikofunika kuyang'anira ana nthawi zonse:

- Kuti akhale otetezedwa.
- Kuti asamazunzidwe ndi kumenyedwa ndi anzawo
- Kuwonetsetsa kuti ana onse adzitenga nawo mbali mmasewero ndi zochitika, kuphatikizapo ana olumala ndi ena omwe atha kusatengapo gawo paokha.
- Kuti muone khalidwe la ana kwa anzawo. (ngati ena akuonetsa khalidwe loyipa, aleziayenera kulowererapo kuti zimenezo zitsachitike)
- Kuonetsetsa kuti ana akuchita molondola zinthu zomwe awudzidwa kuti achite (ngati akukanika, aleziawathandize)

**2. Kufunsa:** Ayikeni ophunzitsidwa mmagulu ang'onoang'ono kapena akhale awiriawiri ndikuwafunsa zomwe angachite atawona zinthu zotsatirazi:

- Mwana akumenya mnzake.
- Mwana akuyankhula zinthu zonyoza kwa mwana olumala.
- Mwana atakhala payekha koma akulira.
- Mwana akukanika kusamba mmanja moyenera.
- Mwana akusewera koma mosakhala bwino pa choseweresa chotererека.

Funsani gulu lililonse kuti lifotokoze kugulu lonse zomwe lakambirana

**3. Kufotokoza:**

- Ophunzitsidwa asamenye ana ngakhale kuti mwanayo walakwisa. Asamagwiritse ntchito mawu owonetsa kukwiya, kuopseza kapena kusalemekeza mwana akalakwisa. Koma ayenera kulongosola bwinobwino kwa mwana uja kumuunikira chifukwa chomwe zomwe wachita ndizoipa ndikumulangiza mwachikondi ngati mwana.
- Ngati mwana akukanika kuchita zomwe wauzidwa kuti achite, muwonetseni mwanayo mmene ntchitoyo imachitikira; komanso muthandizeni mwanayo kuti aphunzire kutero potsata ma sitepe akachitidwe ka ntchitoyo.

**4. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 13: Zochitika mkalasi ya mmera mpoyamba

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa athe kufotokoza ndondomeko zoyang'anira kalasi m'sukulu za mmera mpoyamba

**1. Kufotokoza:** Kuyang'anira kapena kutsogolera kalasi mothekera ndikuchitisa zinthu izi:

- Makalasi ansangala momwe ana onse akusangalatsidwa ndi kuphunzira.
- Kalasi la bata ana onse akuonetsa khalidwe labwino.
- Kalasi lochitachita lomwe ana onse akuphunzira.
- Kalasi la ukhondo komanso lopatsa chikoka.

**2. Kufotokoza:** Kutsogolera kalasi mothekera kutha kukwaniritsidwa ngati:

**a.** Pali zochitika zobwereza/zachizolowezi. Mwachitsanzo, payenera kukhala zochitika zachizolowezi pa nthawi izi:

- Poyamba komanso pamapeto pa tsiku lililonse (ana akamabwera komanso akamachoka ku sukulu).
- Pomwe ana akufuna kupita ku chimbuzi.
- Ana akamafuna kulowa kapena kutuluka mu kalasi.
- Ana akafuna kufunsa funso.

**Kufunsa:** Wonani zithunzi za ana ali pamzere kufuna kusamba mmanja. Iyi ndi ntchito yachizolowezi komanso yomvetsetseka bwino. Ana akudziwa zoyenera kuchita.

**b.** Njira zodalilika zowonetsa utsogoleri pa khalidwe. Aphunzitsi akhale ndi mfundo zomveka bwino zolimbikitsira khalidwe labwino ndi kuletsa khalidwe loipa. Njira zimenezi zisakhale zomenya, kuchitisa manyazi kapena kuvulaza ana.

**Kufunsa:** Wonani chithunzi cha aleziakuyamikira mwana chifukwa choonetsa khalidwe labwino. Iyi ndi njira yodalirika yowonetsa kutsogolera kwabwino pa nkhani ya chikhalidwe.

**c.** Ndondomeko za mkalasi. Payenera kuti pakhale ndondomeko za:

- Kudziwa za ana omwe abwera tsiku ndi tsiku ku sukulu.
- Kupanga chiganizo kuti ana akhale mkalasi.
- Kuonetsetsa kuti makalasi ndi a ukhondo.
- Kusunga mbiri ya mmene mwana akuchitira mu kalasi/ku sukulu.
- Kusunga bwino zipangizo zophunzilira komanso kuphunzilira.


**Kufunsa:** Wonani chithunzi cha ana akupukuta zidole zawo. Izi zikuthandauza kuti pali ndondomeko yomwe yakhazikitsidwa kuti pa sukulu padzikhala pa ukhondo komanso kuti zosewerera ana ndi za ukhondo.

**3. Kufunsa:** Ndizinthu ziti zachizolowezi zomwe zinakhazikitsidwa pa sukulu zawo?

- Ndi njira zanji zomwe zinayikidwa kuti pakhale khalidwe labwino?
- Ndi ndondomeko zanji za m'kalasi zomwe zinayikidwa?

Ophunzitsa alembe mfundozi pa filipichati kapena pa bolodi. Ophunzitsidwa afunsidwe mmene angachitire kuti mfundozi zikhale zodalilika.

**4. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?


1 + 1 = 2
2 + 2 = 4
3 + 3 = 6
Aa
Bb
Cc
Dd
Ee
1
4
5
6
7

# Gawo la ndondomeko 14: Kuwonetsetsa kuti ana olumala akutengapo mbali mu zochitika msukulu ya mmera mpoyamba*

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa athe kunena njira zodalilika zophunzitsira komanso kuphunzirira
- Ophunzitsidwa athe kufotokoza mwa tsatanetsane mmene njirazi zingagwirire ntchito

**1. Kufotokoza:** Ndizofunika kwambiri kuti ana olumala adziwerengeredwa mu zochitika zonse za mmera mpoyamba.

Ophunzira azikambirana njira zofunikira zisanu zophuntsira komanso kuphunzirira.

- **Kumvana/kulumikizana.** Mutha kuyankhula motani kuti mulumikizane kapena mumvane ndi mwana kuti amvetsetse zomwe mukunena komanso kuti akhale ndi chidwi pa zomwe mukuyankhula?
- **Kukonza zochitika**. Ganizirani zochitika zonse za maphunziro a mmera mpoyamba. Mutha kuchita chani kuti zochitikazi zikhale zotsangalasa komanso zachiphunzitso kwa ana pa sukulu yanu? Muchita chani kuti ana onse azitha kutengapo mbali pa zochitikazi, kuphatikizapo ana omwe amaphunzira movutika?
- **Kupeza zipangizo.** Ndizipangizo zanji zophunzitsira ndi kuphunzirira zomwe mungafune kuti zochitika zanu zikhale zotsangalasa komanso zopasa chidwi? Mufuna zipangizo zotani? Muzipeza bwanji? Mukazisunga kuti? Osaganizira zipangizo zogwirika zokha ayi – monga ma buku, zojambulira, zidole – ganiziraninso zinthu zina monga anthu, mwachitsanzo, anthu othandizira (ma volontiya).
- **Kusiyanisa.** Kusiyanisa kukuthandauza kuchitapo kanthu pa zofuna za ana mu kalasi mwanu. Mwachitsanzo, mutha kuchita kuti ntchito ikhale yophwekerako kwa ana ena. Muyeneranso kupereka chithandizo chapadera kwa ana ena payekha payekha ngati ntchitoyo yikuwavuta. Mungakwanise bwanji kuchita izi ngati kalasi yanu yili ndi ana ambiri?
- **Kuyeza ndikupereka zotsatira.** Kodi mungayeze bwanji mmene ana akuchitira pa sukulu yanu ya mmera mpoyamba – makamaka kuwona zomwe ana akudziwa kale ndi kudziwa zomwe ayenera kuti adziwe? Zotsatira zomwe mwapezazo, mungazipereke bwanji kwa makolo mmene ana awo akuchitira?

**2. Kufunsa:** Ayikeni alezimmagulu asanu ndikuwafunsa kuti akambirane ndondomeko zatchulidwa pamwambazi ndikufotokoza kwa gulu lonse.

Funsani magulu ena kuti ayikepo ndemanga zawo ndinso kuwonjezera mfundo zina.

- Mwachitsanzo, mfundo yolumikizana kapena kumvetsetsana; kuyankhula momveka bwino; kulumikizana kogwiritsa ntchito mawu (monga kukweza kapena kutsitsa mawu, kuyankhula mwa pang'ono kapena mokuwa); kugwiritsa ntchito zizindikiro; kukamba nkhani pofuna kunena mfundo ina; kupereka zitsanzo; kulemba mfundo zofunikira kwambiri pa filipichati kapena bolodi; kufunsa mafunso (ngati njira yodziwira ngati zinthu zamveka bwino); kufunsa ana kuti achite ntchito inayake (kuyeza ngati amva); kukamba tizifanizo tosekesa; kuyankhula mchiyankhulo cha makolo; kugwiritsa chiyankhulo chosavuta; kuwonetsesa kuti ana sakupanga phokoso komanso ali tcheru musanayambe kuyankhula; kuyankhula kwa kanthawi kochepa (kuti ana asasiye kukhala ndi chidwi); kuwonetsetsa kuti ana akusangalala komanso kumasuka (kuti akhale ndi chidwi kwambiri kuti apitilize kumvetsera)

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?

* Mutha kuchita phunziro ili kwa ma sabata angapo chifukwa pali zinthu zambiri zofuna kukambirana

Kupeza zipangizo

Kusiyanisa

Kulumikizana

Kuphunzitsa ndi kuphunzira kodalilika

Kuyesa ndi kusunga mbiri kapena kachitidwe

Kusankha zochita

# Gawo la ndondomeko 15: Kuwonetsetsa kuti mwana wa vuto la kuwona akutengapo mbali[2]

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa ndiodzindikira njira zomwe angatsate kuti mwana wa vuto la kuwona azikhala nawo pa sukulu za mmera mpoyamba

**1. Kufunsa:** Ophunzitsidwa angoganiza kuti pa sukulu yawo pali mnyamata dzina lake Daliso amenene ali ndi vuto lakuwona. Amaona ndithu chabe Amaona zochepa kuyerekeza ndi ana ena.

Ophunzitsidwawa apereke njira zomwe zingathandize mwanayu ndipo azilembe pa filipichati kapena pa bolodi.

- Muonetsetse kuti mwanayo wakayezedwa maso ndipo kuti ali ndi magalasi ndi chithandizo cha mankhwala choyenera.
- Onetsetsani kuti a dokotala amene akuyeza maso apereka momveka bwino uphungu womwe utsatidwe kuti Daliso azithandizidwa moyenera kunyumba, mmudzi, ndinso ku sukulu ya mmera mpoyamba. Onetsetsani kuti uphungu umenewu waperekedwa kwa makolo a Daliso, aleziku sukulu ndinso anthu ena ofunikira.
- Pa tsiku loyamba, muwonetseni malo onse a sukulu kuti adziwe mmene palili ndinso adziwe pomwe pamapezeka zomwe angafune.
- Mukamalemba pa bolodi, lembani zimalembo zazikulu zooneka bwino (ananso ena apindulanso nawo).
- Onetsetsani kuti Daliso akukhala pafupi ndi bolodi.
- Onetsetsani kuti zowerenga zomwe Daliso angafune kuwerenga ndizolembedwa mzilembo zazikuluzikulu.
- Onetsetsani kuti m'kalasi mulibe phokoso kuti Daliso athe kumva zomwe ena akuyankhula.
- Onetsetsani kuti ana ena akumuthandizira Daliso mkati komanso kunja kwa sukulu.
- Mpezereni mayendedwe kupita komanso kuchokera ku sukulu (ngati akupezana ndi vuto la mayendedwe).
- Werengani mokweza mawu zinthu zomwe zalembedwa pa bolodi kuti mwina mwana sakuwona bwino zomwe zalembedwa.
- Phunzirani ndondomeko yothandizira kuwona ndinso phunzisani anzanu ena aleziza njirayi.[3]
- Funsani ogwira ntchito za maso mdera lanu kuti abwere ku sukulu ya mmera mpoyamba kuti azakambirane ndi ogwira ntchito kusukulu'ko. Iyeyo atha kufotokoza njira zabwino zomwe ogwira ntchito yaleziatha kugwiritsa ntchito pomuthandiza Daliso.
- Onetsetsani kuti pomwe pakhala Daliso mu kalasi pali kuwala kwa mulingo wabwino (osati kuwala kwambiri, komanso osati kuwala pang'ono) kuti athe kumawona bwino.
- Muzimuyankhulisa Daliso komanso makolo ake pafupi-pafupi.
- Muzimuyamikira ndi kumulimbikisa pomwe wachita chinthu chofunika kuyamikira ndi kulimbikitsidwa.
- Onetsetsani kuti ana ena akumuthandizira Daliso ndipo akumachita naye masewera limodzi.
- Mudzimuyang'anira Daliso mkati ndi kunja kwa sukulu komwe ndikuonetsetsa kuti chilichonse chilli mmalo mwake.

**2. Kukambirana:** Wonani zithunzi pa tsamba lotsatira zowonetsa njira zosiyansiyana mmene Daliso angatengere nawo mbali pa sukulu. Njira zothandizira Daliso kuti atengepo mbali zipinduliranso ana ena. Mwachitsanzo, ana onse atha kupindula ngati mu kalasi mulibe phokoso poti aliyense azitha kumva zomwe osamalira ana akunena.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?


1 2 3
4 5 6

# Gawo la ndondomeko 16: Kuwonetsetsa kuti mwana wa vuto la kumva akutengapo mbali

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa akutha kudziwa ndondomeko zoonetsetsa kuti mwana amene ali ndi vuto la kumva akutengapo gawo pa sukulu za mmera mpoyamba.

**1. Kufunsa:** Yerekezani kuti pali mwana mtsikana wotchedwa Mphatso pa sukulu yanu. Mwanayu ali ndi vuto lokumva. Ngakhale kuti pali mwayi oti atha kumamva zambiri, amamva zochepa kuyerekeza ndi ana ena. Mwachitsanzo, pokhapokha munthu akuyankhula mokweza mawu, iyeyo sangamve bwinobwino. Ngakhale kuti oyankhula akuyankhula momveka bwininobwino, Mphatso sangamve chilichonse ngati enanso akuyankhula nthawi yomweyo.

Ophunzitsidwawa afunsidwe kupereka njira zomwe angagwiritse ntchito kuti Mphatso apezeke akutengapo nawo gawo pa sukulu yawo. Lembani mfundo zawo pa filipichati kapena bolodi.

- Onetsetsani kuti Mphatso wakayezedwa ku chipatala
- Onetsetsani kuti dokotolo oyeza makutu wapereka uphungu womveka bwino mmene Mphatso angathandizidwire ku nyumba, kumudzi ndi ku sukulu ya mmera mpoyamba. Onetsetsani kuti uphungu'wu waperekedwanso kwa makolo, alezipa sukulu komanso kwa anthu ena ofunikira.
- Musanayambe kuyankhula, onetsetsani kuti Mphatso ali tcheru kufuna kumvera.
- Osatseka pakamwa mukamayankhula
- Onetsetsani kuti zomwe mukuyankhula zikumveka bwino kwa Mphatso. Mukayamba kuyankhula phunziro lina, wonetsetsani kuti Mphatso wadziwa kuti mukutero.
- Chepesani phokoso mu kalasi. Ngati muli phokoso, pakhala povuta kuti Mphatso athe kukumvani.
- Mukamayankhula onetsetsani kuti mukumuyang'ana Mphatso ndipo muyesese kuti musamachose maso anu pa iyeyo.
- Yankhulani momveka bwino; phatikizani ndi zizindikiro za kuyankhula kopanda mawu kuti mumveke bwino
- Musayime pa windo kuti nkhope yanu idziwoneka bwino. Ngati pali mthunzi pa nkhope yanu, mpovuta kuti Mphatso awone mmene milomo yanu ikuyendera mukamanyakhula. Khali mwakuti nkhope yanu idziwoneka bwino.
- Gwiritsani zizindikiro zothandizira kuyankhula – mwachitsanzo, mutha kuphunzitsa mogwiritsa ntchito zithunzi.
- Yankhulani momwe mumayankhulira nthawi zonse. (Kuyankhula pango'ono-pang'ono sikuthandiza kalikonse).
- Onetsetsani kuti anthu asamayankhule mwachisawawa koma mmodzi-mmodzi kuti Mphatso asasokonekere.
- Yankhulanani ndi Mphatso komanso banja lakwawo pafupi-pafupi kuti akhale wansangala komanso kuti aziphunzira bwino.
- Yesani kupeza komwe chithandizo cha makutu chimapezeka cha ana ngati Mphatso. Chipatala cha makutu chiliko? Kodi kuli aphunzitsi a luso lapaderadera lophunzitsa ana avuto la kumva ngati Mphatso? Anthu ngati awa angathandize mmene Mphatso angatengere nawo gawo la ndondomeko pa sukulu za mmera mpoyamba.

**2. Kukambirana:** Wonani zithunzi pa tsamba lotsatira zowonetsa njira zomwe zingagwiritsidwe ntchito kuti Mphatso atengepo nawo gawo pa sukulu'zi. Zambiri mwa njirazi zipinduliranso ana ena. Mwachisanzo, ngati mukuyankhula momveka bwino, ana enanso apindula nawo.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 17: Kuwonetsetsa kuti mwana waulumali wa ziwalo akutengapo mbali

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa akutha kunena njira zomwe angagwiritse ntchito kuti mwana wolumala adzitengapo mbali m'sukulu za mkombba phala

**1. Kufunsa:** Yerekezani kuti pali mwana wammuna dzina lake Yohane pa sukulu yanu ya mmera mpoyamba yemwe ali ndi vuto la kuyenda komanso kugwiritsa ntchito manja ake.

Ophunzitsidwa anene njira zomwe angachite kuti amthandizire Yohane. Lembani njirazo pa filipichati kapena bolodi.

- Onetetsani kuti Yohane wakayezedwa kuchipatala kuti mutsimikizike za vuto lomwe ali nalo.
- Funsani dotolo woyezayo kuti apereke uphungu womveka bwino wokhuzana ndi momwe Yohane angathandiziridwe ku nyumba, m'mudzi komanso ku sukulu ya mmera mpoyamba. Uphungu uwu uperekedwenso kwa makolo ake, aleziku sukulu komaso anthu ena ofunikira.
- Fufuzani kwambiri za ulumali wa Yohane ndi momwe ukubweretsera mavuto mu zochita zake. Gawanani ndi anzanu zomwe mwapeza.
- Limbikitsani kuyankhulana mosabisa. Yankhulanani ndi Yohane komanso makolo ake pafupi-pafupi.
- Ngati Yohane angapindule atakhala ndi zipangizo zothandizira, monga ndondo zoyendera, onetetsani kuti wapatsidwa zinthu zoterezo.
- Kodi mipando ya m'kalasi lanu ndiyoti Yohane atha kukhalira mosavuta? Ngati sichoncho, muyenera kuyisintha kuti azitha kukhalira mosavutikira.
- Ngati Yohane akupezana ndi mavuto poyenda popita kapena kuchoka ku sukulu, chilipo chomwe mutha kuchita kuti mayendedwe ake akhale osavuta komanso osapereka chiopsezo?
- Kodi Yohane amatha kuyenda mosavutika komanso mopanda chiopsezo chilichonse pa malo ozungulira sukulu? Zungulirani naye pamalopo limodzi kuti mudziwe ngati amapezana ndi vuto lilonse.
- Kodi zimbuzi ndi malo osambira mmanja zili poti Yohane atha kufikira mopanda vuto? Ngati Yohane atha kupezana ndi vuto kuzifikira, inu ndi anzanu mutha kuchitapo chani kuti mukonze zovutazo?
- Onetsetsani kuti zinthu zomwe zili mu kalasi lanu zayikidwa mwadongosolo. Zitsangokhala balala. Onetsetsani kuti mipando mwayilowesa kunsi kwa tebulo kapena desiki ndiponso kuti zikwama zayikidwa ku malo koyenera. Njira zonse mukhale mopanda zinthu zoti zingabwerese vuto kwa Yohane.
- Ngati Yohane ali ndi vuto kugwira zolembera monga peni, pensulo ndi zigamusa, tengani ka nsalu ndikukutira kunja kwa cholemberacho. Mwanjira ina, mutha kupeza cholembera chomwe chilli chokulirapo.
- Zitha kukhala zothandiza kuti Yohane apatsidwe zolembera zosavuta kugwiritsa ntchito monga maka kuti azitha kulembera pa pepala.
- Ngati Yohane akupezana ndi vuto kutsiriza ntchito yomwe wapatsidwa, mpatseni nthawi yaitali kuti amalize kapena chepetsani ntchitoyo kapenanso mutha kupeza munthu wina kuti ammalizire ntchitoyo.
- Ngati Yohane akupeza vuto kuti atengepo mbali pa zochitika za m'kalasi, konzani zochitikazo kuti zikhale zoti nayenso atha kuchita nawo, kapena sinthani zochitikazo poyambisa zina zoti atha kuchita nawo. Mwanjira ina, onetsetsani kuti ana ena akumthandizira Yohane kuti achite nawo ntchitoyo.
- Mukamachita zinthu ndi mwanayo kapena makolo ake, pezani njira mmene zofuna zake zingakwaniritsidwire (mwachitsanzo, kupita ku chimbuzi).

**2. Kukambirana:** Wonani zithunzi pa tsamba lotsatira. Kodi Yohane akuthandizidwa bwanji kuti atengepo gawo pa sukulu?

**3. Kufunsa:** Kodi ophunzitsidwa aphunzirapo chani pa gawo la ndondomeko ili?



# Gawo la ndondomeko 18: Kuwonetsetsa kuti mwana amene ali ndi vuto lakuphunzira akutengapo mbali

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa akutha kunena njira zomwe angathandizire mwana amene ali ndi vuto la kuphunzira kutengapo gawo pa sukulu ya mmera mpoyamba


**1. Kufunsa:** Yerekezani kuti pali mwana mtsikana dzina lake Chikondi m'kalasi lanu amene akuvutika kuti aphunzire. Akuwona zovuta kunenapo maganizo ake m'kalasi komanso kuti amve zomwe mukuyankhula. Amavutika kapena kukanika kumene kuchita ntchito zomwe wapatsidwa ngakhale zitakhala zosavuta chotani.

Ophunzitsidwa anene njira zomwe angayike kuti mwanayu athandizike. Lembani njirazo pa filipichati kapena pa bolodi.

- Onetsetsani kuti Chikondi wakayezedwa ku chipatala. Izi zithandira kudziwa za mavuto omwe ali nawo. Funsani woyezayo kuti apereke uphungu womveka bwino mmene Chikondi angathandiziridwe ku nyumba, mmudzi komanso ku sukulu ya mmera mpoyamba. Onetsetsani kuti uphungu umenewu waperekedwanso kwa Chikondi ndi makolo ake.
- Mukhulupirireni. Mwana aliyense ali ndi kuthekera. Mungofunika kuti mupeze njira kuthekera kwake kuwonekere.
- Mulemekezeni. Ana amakula bwino mu zonse ngati akulemekezedwa.
- Muzikonzekera kuphunzitsa. Konzekerani zophunzitsira za chaka chonse, teremu, sabata komanso za tsiku. Mukatero mudzaziwa chomwe mukuchita komanso chifukwa chake.
- Gawani phunziro lanu. Osamuphunzitsa Chikondi zinthu zonse pa kamodzi. Zophunzitsira za chilendo zizibwera pang'ono-pang'ono osati pakamodzi.
- Pophunzitsa, yambani ndi zomwe amadziwa ndikumalunjika ku zomwe samadziwa. Mwachitsanzo, ngati mukufuna kuphunzitsa zokhuzana ndi zachilengedwe, yambani ndi zomwe Chikondi akudziwa ndi ndikuziona nkale.
- Ana asamangouzidwa pophunzitsidwa koma azitha kuwona, kugwira komanso kuchita zomwe akuphunzitsidwa.
- Osangophunzitsa ndikusiyira pomwepo ndikuyamba zina za chilendo ayi. Perekani mwayi kwa Chikondi kuti awonese zomwe waphunzira.
- Perekani chithandizo chofunikira kwa Chikondi akamaphunzira, koma mwa pang'ono-pang'ono siyani kumuthandizira akayamba kudziwa zambiri komanso kudzikhulupirira. Izi zithandizira kuti Chikondi akahale wophunzitsidwa wodzidalira.
- Yang'anirani kuphunzira kwa mwana. Onetsetsani kuti mukudziwa zomwe Chikondi akutha kuchita zomwe amakanika. Llimbikirani kuthandizira zomwe akukanika.
- Myamikireni Chikondi komanso kumulimbikitsa – koma pokhapokha atachita china chake chabwino. Ana akamayamikiridwa pa chilichonse, kuyamikirako kumakhala kopanda ntchito.
- Yankhulani momveka bwino. Ndinjira zanji zomwe mungalumikizirane bwino ndi Chikondi?
- Limbikitsani ana kuphunzitsana okhaokha. Ana ena atha kumafuna kumuthandiza Chikondi kuchi ntchito zina. Izi zikuchepeserani ntchito komanso kupereka mwayi kwa ana kuti azithandizana. Koma ndibwino kuti Chikondi adzichita zinthu zambiri yekha mosadalira anzake.
- Muthandizeni Chikondi payekha. Ngati mwatanganidwa kwambiri kuti simungathe kutero mu kalasi, mutha kutero nthawi ina yosakhala ya kalasi?
- Pezani nzeru kwa anzanu. Kodi alezianzanu sangakugawireni uphungu mmene mungasamalire ana monga Chikondi kutengera kuti iwo anagwirapo kale ntchito monga imeneyo? Lumikizanani ndi makolo a Chikondi. Atha kukupasani uthenga ofunikira. Atha kuthandiziranso ngati kuwonjezera pa zomwe mukuphunzitsa ku sukuklu. Nonse pamodzi mutha kuthandiza mwanayu.

**2. Kukambirana:** Wonani zithunzi pa tsamba lotsatira lowonetsa mmene Chikondi angathandiziridwe kuti azichita nawo sukulu za mmera mpoyamba. Ana enanso ambiri pa sukulu yanu apindula nawo ndi njira zophunzitsirazi, osakhala Chikondi yokha.

**3. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani mu gawo la ndondomeko ili?


1 2 3 4 5

# Gawo la ndondomeko 19: Kulumikizana ndi kugwirira ntchito limodzi

## Zotsatira:

- Ophunzitsidwa athe kutchula anthu ndi ma bungwe omwe atha kuthandizira kuti ana omwe ali ndi ulumali aziyimba nawo sukulu ya mmera mpoyamba.
- Ophunzitsidwa athe kutchula njira zomwe anthu ndi ma bungwe'wa angagwiritse ntchito pothandizira.

**1. Kufotokoza:** Zitha kukhala zosavuta kuti ana omwe ali ndi ulumali aziyimba nawo sukulu za mmera mpoyamba ngati pali kugwira ntchito limodzi. Ndi kofunika kugwirizana ndi kuthandizana pogwira ntchito zokhudzana ndi ana olumala.

**2. Kukambirana:** Wonani zomwe zajambulidwa pa tsamba lotsatira. Zimenezo zikuonetsa ma bungwe ndi anthu onse omwe atha kuthandizira Sukuluzi kuti zizikhalanso ndi ana omwe ali ndi ulumali.

**3. Kufunsa:** Nthawi ya zokambirana, funsani ophunzitsidwa kuti atchule zomwe anthu okhudzidwa ndi ma bungwe angathandizire.

**Komiti za atsogoleri a mmudzi**

- Atha kukakamiza makolo omwe ali ndi ana a ulumali kuti awapitise ku sukulu za mmera mpoyamba
- Kumema anthu kuti athandizire kuti ana omwe ali ndi ulumali nawonso azipita ku sukulu'zi
- Kuthandiza ma sukuluwa ndi zipangizo kapena ndalama kuti zikhale zabwino kwa ana omwe ali ndi ulumali

**Antchito za umoyo**

- Kuthandizira kupeza ana omwe ali ndi ulumali mma sukulu komanso mmidzi
- Atha kulangiza kuti ana oterowo apite akayezedwe ku chipatala
- Kuwonetsetsa kuti ana omwe ali ndi ulumali akupeza chithandizo choyenera cha ku chipatala komanso zipangizo zina zothandizira

**Makolo a ana omwe ali ndi ulumali**

- Kuthandiza ana kuyenda popita ndi kuchoka ku sukulu
- Kuthandizira ma phunziro a mwana ku nyumba
- Kuwonetsetsa kuti mwana akutenga nawo mbali pa zochitika za mnyumba komanso mmudzi
- Kuwonetsetsa kuti mwana akupatsidwa chakudya chabwino komanso akupatsidwa chithandizo ndi chilimbikitso

**4. Kufunsa:** Alipo anthu ndi ma bungwe omwe ayiwalidwa pa zojambula zili apa? Atchuleni ndiponso munene mmene angathandizire kuti ana omwe ali ndi ulumali azitenga na gawo pa sukulu za mmera mpoyamba

**5. Kufunsa:** Ophunzitsidwa aphunzirapo chani mu gawo la ndondomeko ili?


Bungwe loyang'anira anthu omwe ali ndi ulumali (FEDOMA)
Mabungwe oyima pa okha osakhala a boma
Anthu ammidzi
Mabungwe othandiza mayiko osauka pa chituko (Monga Sightsavers)
Sukulu zina za mmera mpoyamba
Sukulu za pulayimale
Mabungwe a za umoyo omwe si aboma
Unduna wa za umoyo (zipatala komanso anthu ophunzitsa za umoyo)
Unduna wa maphunziro
Unduna woona kuti palibe kusiyana pakati pa amuna ndi akazi (pamodzi ndi ogwira ntchito zoyang'anira anthu komanso ogwira ntchito zoyan'ganira ana)
CBCC

# Gawo la ndondomeko 20: Kukonza ndi kusatira ndondomeko yoyendetsera sukulu ya mmera mpoyamba

## Zotsatira:

- Alezi apanga ndondomeko yoyendetsera sukulu kuti yikhale yokomera aliyense.

**1. Kufotokoza:** Ili ndi gawo la ndondomeko lomaliza.

**2. Kufunsa:** Ophunzitsidwa atengapo chani pa maphunziro'wa? Lemba zomwe atchule pa filipichati kapena bolodi.

**3. Kufotokoza:** Mu gawo la ndondomeko ili alemba ndondomeko yomwe adzasate kuti sukulu yawo idzikhala ndi ana onse mosasankha.

- Atchula mfundo zisanu zomwe adzasate mu miyezi iwiri ikubwerayo kuti sukulu zawo zikhale zokomera ana omwe ali ndi ulumali.
- Mfundozi zikasatidwa, ndondomeko ina idzalembedwa yomwe idzanene zomwe zingadzasinthe kutsogolo.
- Fotokozani kuti mfundo zawo zitha kukhala zokhuza mbali iliyonse yomwe akuwona kuti ndiyofunikira. Mwachisanzo, ndondomeko yake yitha kukhuza zinthu ngati izi:
  - > Kupeza ana omwe ali ndi ulumali kuti apititsidwe ku sukulu.
  - > Kulimbikitsa makolo omwe ali ndi ana a ulumali kuti awatumize ku sukulu za mmera mpoyamba.
  - > Kuwonetsetsa kuti ana olumala akupita ku sukulu mosavutika.
  - > Kudziwitsa anthu mmidzi za ufulu wa ana olumala wopita ku sukulu za mmera mpoyamba.
  - > Kudzakambirana za nkhaniyi pa msonkhano wa otsogolera a sukulu ya mmera mpoyamba kapena komiti ya atsogoleri a mmudzi.
  - > Kutengera ana olumala omwe anayamba kale sukulu'zi ku ntchito za umoyo komanso zosamala anthu.
  - > Kuwonetsetsa kuti ana olumala omwe ali kale mu sukulu'zi ali ndi zipangizo zowathandizira (monga njinga za anthu olumala)
  - > Kuwonetsetsa kuti sukulu'zi ndisozapereka chiopsezo komanso kuti ndizofikilika kwa ana olumala.
  - > Kuwonetsetsa kuti ana onse, kuphatikizapo omwe ali ndi ulumali, akupatsidwa phala tsiku lililonse.
  - > Kukhadzikitsa malamulo ndi zochitika zachizolowezi kuti ana onse aziphunzira pamodzi.
  - > Kusata njira zatsopano zolimbikitsira khalidwe labwino pa sukulu
  - > Kuthandiza mwana amene ali ndi ulumali kukayamba sukulu ya pulayimale.
- Awuzeni apeze mfundo kapena ntchito zolozeka ndi njira zomwe angayezere ngati mfundozo kapena ntchitozo zakwaniritsidwa kapena ayi.

**4. Kufotokoza:** Awonetseni chitsanzo cha ndondomeko ya sukulu za mmera mpoyamba yomwe yili pa tsamba lotsatira ngakhale kuti ndiyosatha kwenikweni.

Yimalizitseni nonse pamodzi.

# Ndondomeko yoyendesera sukulu ya mmera mpoyamba

<table>
<tr><td colspan="3">Cholinga: Kuwonetsetsa kuti kuphunzira ndi kuphunzitsa zikukomera ana onse pa sukulu yathu</td></tr>
<tr><td>Dzina la sukulu</td><td colspan="2">Chiradzulu CBCC, Blantyre</td></tr>
<tr><td>Alezi</td><td colspan="2">Mrs. Asale; Mr. Mtima; Mr. Kwacha; Mrs. Sigele; Mrs. Chalamanda</td></tr>
<tr><td colspan="2">Tsiku loyambira</td><td>Tsiku lomaliza: (nthawi: miyezi iwiri)</td></tr>
<tr><td colspan="2">Tisintha zinthu izi kuti sukulu yathu yikhale yokomera ana onse (sankhani mfundo zisanu ndipo wonetsesani kuti mfundozo ndizomveka bwino).</td><td>Tidziwa bwanji kuti mfundozi zakwaniritsidwa (zizindikiro zowonetsa kuti zakwaniritsidwa)?</td></tr>
<tr><td colspan="2">1. Tidzisesa malo onse a sukulu kuti akhale a ukhondo komanso osapereka chiopsezo kwa ana onse</td><td>1. A Asale aziyang’anira malo a sukulu tsiku lililonse kuwonetsetsa kuti palibe zinyalala</td></tr>
<tr><td colspan="2">2. Zosewerera zonse zidzisungidwa mu kabati</td><td>2. A Mtimawill aziwonetsetsa kuti pamepeto pa tsiku, zipangizo zonse zasungidwa malo oyenera</td></tr>
<tr><td colspan="2">3. Tidziwonetsetsa kuti Gloria, mtsikana amene ali ndi vuto la kuwona adzikhala kutsogolo mu kalasi kuti azitha kuwona alezi komanso kuti aphunzitsi adzimuwona ndi kumuthandiza ngati ndikofunika kutero.</td><td>3. A Kwacha, omwe amathandira Gloria azilemba ndi kusunga zonsezi</td></tr>
<tr><td colspan="2">4.</td><td>4.</td></tr>
<tr><td colspan="2">5.</td><td>5.</td></tr>
<tr><td colspan="3">Ena okhuzidwa ofunika kugwira nawo ntchito limodzi komanso kudziwitsidwa ndi awa:Otsogolera sukulu (CBCC); Komiti ya atsogoleri a mmudzi;<br>Mayi ndi bamboo a Gloria</td></tr>
</table>

# Sources

Ministry of Gender, Children, Disability and Social Welfare [MoGCDSW], 2014. National Syllabus for Integrated Early Childhood Development. MoGCDSW/World Bank: Lilongwe.

Ministry of Gender, Children Disability and Social Welfare [MoGCDSW], 2017. National Policy on Early Childhood Development: Breaking the Intergeneration Cycle of Poverty. MoGCDSW: Lilongwe.

UNESCO/International Bureau of Education [IBE], 2016. Reaching Out to All Learners: A Resource Pack for Supporting Inclusive Education. IBE-UNESCO: Geneva.

# References

**1.** Wonani UNESCO-IBE (2016).

**2.** Ndondomeko imeneyi ndiyothandizira ana omwe ali ndi vuto la kuwona kuti ayende kuchoka malo amodzi kufikira pena. Bungwe la Sight Savers ili ndi tsamba lophunzitsira za ndondomekoyi lomwe mutha kupatsidwa. Mutha kulipeza pa: https://www.sightsavers.org/reports/2017/10/assisting-children-visually-impaired/